NYA_TTB_0914_20160929_script

**Filemoni : 1-25**

**Mutu : Kuonetsedwa kwa chikondi cha Kristu kwa ife ndi kuonetsa momwe chikondi chapa abale chiyenera kuyendera**

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu, anzanga apaulendo. Lero, tiyeni titsogozedwe ndi mau apa Yesaya 64:6, amene akuti, "Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati chobvala chodetsedwa; ndipo ife tonse tifota monga tsamba, ndi zoipa zathu zitiuluza monga mphepo."

Tsono lero m'kalata ya Filemoni, tikambirana za kuonetsedwa kwa chikondi cha Kristu kwa ife ndi kuonetsa momwe chikondi chapa abale chiyenera kukhalira. Ili, ndi buku lina la m'Chipangano Chatsopano, yomwe ndi kalata ina, yofunika kwambiri m'mau a Mulungu.Ndiye pamene tiwerenga kalata imeneyi, tipeza kuti ndiyo kalata yamwini, koma taonani kuti Mzimu Woyera anainayenereza kukhala gawo limodzi la mau a Mulungu.

Tsono Paulo akulemba kalata iyi, kwa Filemoni chifukwa cha nkhani yomwe inachitikira Filemoniyo. Koma poyamba tiyeni tione

kuti Filemoni anali kukhala kumalo otchedwa Kolose. Awa, ndimalo amene ali m'dziko la Firigiya, dziko lomwe lero lino likutchedwa Turkey. Ndiye kalata iyi, inalembedwa pambiri yokhudza ukapolo wa anthu akuda. Taonani mu Roma munali akapolo ochuluka okwanira 60 million, pamene anthu onse a mu Roma sanali kupitilira 100 million.Uku ndikutsimikiza kuchuluka kwa chiwerengero cha akapolo m'nthawi ya Paulo.

Ndiye mu mzinda wa Kolose, munali munthu wina wolemera wotchedwa Filemoni, amene anakhulupirira Kristu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wa moyo wake. Iyeyu, anali ndi kapolo wotchedwa Onesimu, amene anathawa kwa mbuye wake, naganiza kuti anali paufulu, koma anazindikira kuti Paulo, amene anali muunyoro ndiye amene anali paufulu weni-weni, koposa iye amene analibe unyolo. Ichi, ndichimene chidamukakamiza Onesimu kuti akafunse Paulo chinsinsi cha ufulu wake. Paulo anamuuza kuti ndi kukhulupirira muimfa ndi kuuka kwa Yesu Kristu ndiko kumene kunamupatsa mtendere. Tere, Onesimu anakhala cholengedwa chatsopano mwa Kristu Yesu.

Koma Onesimu, monga munthu wina aliyense wotembenuka mtima kumene, anali kuganizira za moyo wake wakale, kotero kuti anabwerera kwa Paulo namuuza kuti anali kapolo wothawa wa Filemoni, ku Kolose. Tsono Paulo poona kuti Filemoni anatembenukanso mtima kudzera mwa iye, anamuuza kuti abwerere kwa mbuye wake, koma atatenga kalata iyi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyenera kuzindikira kuti mumtima wa munthu muli chilako-lako chofuna kukhala paufulu.Koma taonani kuti m'dziko lathu lino, ngakhale tiri ndi ufulu wodzilamulira, koma anthu ochuluka ndi akapolo auchimo; amoyo wauhule, akapolo a chuma ndi uchimo wosiyana-siyana. Iwowa, amaganiza kuti ali aufulu, koma taonani Ambuye Yesu pa Yohane 8:36, akunena kuti, "Chifukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu aufulu, mudzakhala mfulu ndithu." Kodi inu Mwana wa Mulunguyo, adakumasulani kale ku msinga za uchimo?

Tsono cholinga chachikulu cha kalata iyi, ndikuonetsa chikondi cha Kristu kwa ife tonse, poona zomwe anatichitira, pokhala wochimwa pamaso pa Mulungu m'malo mwathu. Tere kalata iyi, ikuonetsa chitsanzo chokoma, momwe munthu wina akulandira

chilango m'malo mwa wina. Tamvani Paulo pa verse 17, akunena kuti, "Ngati tsono undiyesa woyanjana nawe, umlandire iye monga ine mwini." Kutsimikiza kuti Kristu ndiye anaimira ife pamaso pa Mulungu, popeza ife tilibe chotiyenereza kwa Mulungu. Tere, pano tikuona kuti Onesimu, kapolo wothawa amayenera kulandiridwa monga momwe Paulo, amene anali mtumiki wamkuru, akanalandiridwira.

Ndiye kudzera kuchitsanzo chimenechi, Paulo anaganiza zoonetsa chikondi chapa abale. Mu kalata ino, Paulo akuonetsa momwe chikondi chapabale chiyenera kuyendera. Tere, taonani kuti Onesimu ndi Filemoni, ndiwo anthu amene anali m'magulu awiri osiyana, amene anali kudana komanso kupwetekana, koma pano ndiwo abale chifukwa cha Kristu ndipo ayeneradi kuchita monga abale.

1. Paulo, wandende wa Kristu Yesu, ndi Timoteo mbaleyo, kwa Filemoni wokondedwayo ndi wa ntchito mnzathu.

Poyamba ndifuna muone kuti Paulo sakutchula kuti ndiye Mtumwi ayi, popeza akulemba kalata iyi kwa munthu pa yekha. Mukumbukira kuti pamene anali kulemba kalata ku mpingo, anali

kugwiritsa ntchito dzina la udindo wake, kuti Mtumwi wa Yesu Kristu. Iye anafunitsitsa kuti kalata iyi, ikhale ya munthu pa iye yekha, koma taonani lero ikuwerengedwa padziko lonse lapansi. Koma pano Paulo akunena kuti ndiye kapolo wa Kristu. Kutanthauza kuti ali wake wa Kristu, kotero kuti akhoza kumugwiritsa ntchito monga afuna ndipo kuti zinthu zonse kwa iye zimachitika mwachifuniro cha Kristu.

2. Ndi kwa Apiya mlongoyo, ndi Arkipo m'sirikari mnzathu, ndi kwa mpingo uli m'nyumba yako.

Poyamba ndifuna ndinene kuti Apiya, anali mkazi wake wa Filemoni. Tsono popeza dzina la Filemoni ndi la chigiriki, likutanthauza kuti iyeyu, monga munthu wa business, anapita ku Kolose chifukwa cha malonda ake, kumene anakakumanako ndi Apiya, namukwatira. Koma chinthu chochititsa chidwi ndi chakuti onse awiriwa, anatembenuka mtima pautumiki wa Paulo, kotero kuti mpingo unali m'nyumba yawo.Ndiye Paulo akumutchula Filemoni kuti ndi wantchito mnzake komanso kuti ndiye m'sirikari mnzake, kutanthauza kuti atumiki a Mulungu ayenera kumadziona kuti ndiwo antchito komanso asirikari, amene ayenera

kukhetsathukuta ndi kumva kuwawa.Iwowa, ayeneransokukhala tcheru,kugwirizana, kudalirana ndi kulimbikitsanapantchito yawo yopatulika.Komanso pamene Paulo akunena kuti mpingo unali m'nyumba yawo, akutanthauza kuti mpingo, uyenera kuyambira m'nyumba kapena m'banja.Kodi m'banja lanu, mumamveka kapena kuchitika mapemphero?

4. Ndiyamika Mulungu wanga nthawi zonse, ndi kukumbukira iwe m'mapemphero anga.

Ndime ino, ikuonetsa zinthu zingapo zofunika kwambiri; choyamba tikuona kuti Paulo anali ndi chizolowezichokumbukiramipingo komanso anthu ena, m'mapemphero ake.Kachiwiri, tikuona kuti ngakhale Paulo anali m'ndende, koma anali ndi nthawi yopemphera pa iye yekha.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti ngakhale Paulo anali womangidwa, koma anali mfulu mumtima, chifukwa anali kukumbukira abale ake m'chikhulupiriro chawo, amene anali kutari ndi iye.Tsono chikondi chimene Paulo akuonetsachi, zikutsimikiza kuti analidi munthu wokonda kupemphera komanso

wachikondi chapa abale.Kodi inu mulinawo mtima wopempherera ena?

5. Pakumva za chikondi chako ndi chikhulupiriro uli nacho chakulinga kwa Ambuye Yesu, ndi kwa oyera mtima onse;
6. Kuti chiyanjano cha chikhulupiriro chako chikakhalechamphamvupodziwa chabwino chiri chonse chiri mwa inu, cha kwa Kristu.

Pano tikuona kuti moyo wa Filemoni unali wachitsanzo chabwino wokonda Ambuye Yesu, komanso wokhulupirira anzake. Komanso anali ndi chikhulupiriro chakwa Ambuye ndi kwa wokhulupirira anzake. Kutsimikiza kuti Filemoni anali ndi chikhulupiriro komanso chikondi chogawana ndi anzake.Ichi, ndichotsatira cha ntchito yomwe Ambuye amachita mwa wokhulupirira. Tamvani; Paulo pa Afilipi 2:13, akunena kuti, “Pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe, chifukwa cha kukoma mtima kwake, ndiye Mulungu.”

7. Pakuti ndinalinaco chimwemwe chambiri ndi chisangalatso pa chikondi chako, popeza mitima ya oyera mtima yatsitsimuka mwa iwe, m’bale.

Paulo mundime ino, akuonetsa kuti anali ndi chimwemwe chambiri komanso chitonthozochifukwa cha chikondi cha Filemoni pa anthu ena ndi pa Paulo.Ndikunena mau amenewa chifukwa cha mau akuti, “popeza mitima ya oyera mtima yatsitsimuka mwa iwe, m'bale.” Kutanthauza kuti pamene mitima ikutchulidwa, zikutanthauza kuti nkhani ikuchokera kwa munthu wathunthu. Kutsimikiza kuti moyo wa wokhulupirira ena, unali wokhutitsidwa mwa Filemoni.Kodi inu akristu anzanu amapezachitonthozo kapena kukwanitsidwa mwa inu?

8. Momwemo, ndingakhalendirinakokulimbika mtima kwakukuru mwa Kristu kukulamulira chimene chiyenera,
9. Koma Makamaka ndidandaulira mwa chikondi, pokhala wotere, Paulo nkhalamba, ndipo tsopano wandendensowa Kristu Yesu.

Pano tikuona Paulo akupempherera Onesimu.Ichi, ndicho cholinga cha kalata ino. Taonani iye akupereka pempholake mwaubwino, mwaubale ndi chikondi. Pachifukwa chimenechi, Paulo akupemphamogwiritsa ntchito zifukwa zitatu; poyamba Paulo akupempha chikhululukiro cha Onesimu pachifukwa cha chikondi

cha iwo eni monga wokhulupirira mwa Kristu Yesu. Kachiwiri, Paulo akupempha popeza tsopano anali atakalamba chifukwa cha kuzunzika monga mtumiki wa Kristu. Kachitatu, Paulo akunena kuti Filemoni amumvetsetse pa pempho lake pokhala iye anali wandende, kotero kuti sakanathakumasulidwa kuti akalankhulenaye pamaso ndi pamaso.

10. Ndikudandaulira chifukwa cha mwana wanga, amenendam'bala m'ndende, Onesimu,
11. Amene kale sanakupindulira, koma tsopano watipindulira bwino iwe ndi ine.

Paulo akupempherera mwana wake Onesimu, kapolo wothawa, amene anatembenuka mtima. Taonani Paulo nthawi imeneyi mkuti alibe mkazi, koma anali ndi ana ambiri monga Timoteo, Tito ndipo pano akumutchula Onesimu kuti ndiye mwana wakenso.Kutsimikiza kuti onsewa anali ana ake mumzimu. Taonani Onesimu ndiye mwana wake, amene anam'balaali m'ndende. Kutsimikiza kuti Paulo anamutsogolera Onesimu kwa Ambuye pamene anali m'ndende.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone zinthu ziwiri mundime ino; poyamba ndifuna muone kuti Paulo anali munthu wochenjera pakupereka pempho limeneli.Taonani akutchula Onesimu kuti ndiye mwana wake.Kutanthauza kuti kunali kobvuta kuti Filemoni akanepempho lake chifukwa chotchula kuti ndiye mwana wake. Kachiwiri; tikuona kuti pamene Paulo akunena kuti Onesimu kuti ndi mwana wake, akutanthauza kuti mau a Mulungu salimbikitsa nkhani yaukapolo ayi, komanso kuti anali munthu wokondedwa komanso waphindu. Pachifukwa chimenechi, Paulo samafuna kuti Filemoni akumbukire makhalidwe oipa akale ya Onesimu. Ndiye tikuphunzira kuti kutembenuka mtima ndiko kumasintha moyo wa munthu, kuchoka kumunthuwosapindula, ndi kukhala munthu waphindu kwa Ambuye ndi kwa banja lake. Ichi, ndichifukwa chake Paulo akumupempha Filemoni kuti amulandire osati ngati kapolo, mwana wake.Kodi inu ngati wokhulupirira Ambuye, komanso banja lanu limakudalirani kuti ndinu munthu waphindu?

12. Amene ndi yemweyo ndakubwezera iwe, ndiye mtima weniweniwa ine.

13. Ameneyondikadafuna ine kumsunga akhale nane, kuti m’malo mwako akadanditumikira ine m’ndende za Uthenga Wabwino.

14. Koma wopanda kudziwa mtima wako,sindinafuna kuchita kanthu; kuti ubwino wako usakhale monga mokakamiza, komatu mwaufulu.

Paulo pano akupempha Filemoni kuti amulandire Onesimu monga momwe akadamulandira iye.Taonani kuti Paulo anali ndi mtima wofuna kusunga Onesimu, kuti azimutumikiram’ndendemo, koma sakanatero popanda chilolezoFilemoni.Kutsimikiza kuti Paulo anamuona Onesimu kuti anali wopindula kumoyo wake waukalamba komanso potumikira Kristu, komasamafuna Filemoni kuti apereka Onesimu mokakamizidwa ayi, koma mwa ufulu wake.Ndiyetikafufuzasitikumva kuti Filemoni anamubweza Onesimu kwa Paulo ayi, kutsimikiza kuti Onesimu anakhaladi waphindu.

15. Pakuti kapena anasiyanitsidwa ndi iwe kanthawi chifukwa cha ichi, ndi kuti udzakhala naye nthawi zonse;

16. Osatinso monga kapolo, koma woposa kapolo, mbalewokondewa, Makamaka ndi ine, koma nanga ndi iwe, m'thupi, ndiponso mwa Ambuye.

Pano ndifuna kupereka chidziwitso chakuti, kuyambira nthawi yomwe Onesimu, anakhulupirira Kristu, moyo wake ndi ubale wake ndi Filemoni, mbuye wake unasintha.Koma iyeyu, ndikapolo ndithu malinga ndi malamulo a Roma, ngakhale pano sikapolonsokwa Filemoni. Iye, ndi m'bale kwa Filemoni.

Wokondedwa anzanga apaulendo, mundime ino muli chitsanzo chokoma momwe munthu wosachimwa akulowa m'malo mwa munthu wochimwa.Tamvani Paulo akupempha Filemoni kuti amulandire monga m'bale osati ngati kapolo ayi. Umu, ndimomwe zili ndi Ambuye wathu Yesu Kristu kuti amatipembedzerakwa Atate, kuti atilandire monga momwe angalandire Iye. Kunena kuti pamene munthu wochimwa alapa, amalandiridwa ndi Atate monga momwe Atate amalandira Ambuye Yesu, chifukwa tsopano ali ndi ufulu wokhala mwana wa Mulungu. Iyi, ndiyo nkhani akunena Paulo pa Aefeso 1:5-6, pamene akuti, "Anatikonzeratutilandiridwe ngati ana a Iye yekha mwa Yesu Kristu, monga

umokunakomerachifuniro chake, kuti uyamikidwe ulemerero wa chisomo chake, chimene anatichitira ife kwaufulu mwa Wokondedwayo (Kristu).”

17. Ngati tsono undiyesa woyanjana nawe, umlandire iye monga ine mwini.

Nkhani ikuti, monga Filemoni ali woyanjana ndi Paulo, ayenera kumlandiranso Onesimu ngati woyanjana naye monga momwe ayanjana ndi Paulo.  Kutanthauza kuti zonse zimene Filemoni akhoza kuchitira Paulo, achitirenso Onesimu, chifukwa ndiye m’bale tsopano.Tere, tikuphunzira kuti atumiki anzeru ndi wokoma mtima, amakhala ndi chisamaliro chabwino pa anthu amene angobadwa kumene, ndi cholinga chopereka chilimbikitso pazimene angachite.

18. Koma ngati anakulakwira kanthu, kapena wakongola kanthu, undiwerengere ine kameneko;

Mau a Paulo pano akuonetsa chithunzi cha Ambuye Yesu pa wokhulupirira onse.  Taonani akunena kuti ngati Onesimu anakongola kanthu kwa Filemoni, awerengere pa iye.  Kutanthauza

kuti Paulo anali wokonzeka kubwezangongoleyo m'malo mwa Onesimu.

Taonani pamene munthu wochimwa alapa machimo ake, nthawi yomweyo Ambuye Yesu amanena kuti machimo a munthuyu, awerengedwe pa Iye, popeza anafa pamtanda chifukwa cha machimo a munthuyu. Mwanjira ina Ambuye Yesu amapempha Mulungu Atate kuti alandire munthu wochimwa uja, monga momwe angamulandire Iye. Uthenga uwu, ndiwo pachimake penipeni pa kalata imeneyi.

19. Ine Paulo ndichilemba ndi dzanja langa, ndidzachibwezera ine; kuti ndisanene nawe, kuti iwe ndiwemangawa anga.

Paulo mundime ino, akupereka chitsimikizo chakuti adzabwezangongole iliyonse chifukwa walemba kalatayi ndi dzanjalake. Taonani ichi, ndichimene anachita Ambuye Yesu popereka moyo wake mwakukhetsa mwazi ndi kulipa mlandu wa inu ndi ine.Ichi, ndicho chinthu chimene chiyenera kulimbikitsa inu ndi ine, popeza Kristu ndiye chikole/nkhoswe cha chipulumutso chathu (Ahebri 7:22).Kutsimikiza kuti Kristu,

anakhala wochimwa m'malo mwa inu ndi ine, anthu ochimwa, kuti tikakhale wolungama pamaso pa Mulungu mwa Iye.

Tsono lonjezo lomwe Paulo akupereka chifukwa cha Onesimu, likutanthauza kuti anali kumukonda Onesimu kopambana, komanso kuti anali ndi chitsimikizo chonse kuti anatembenukadi mtima.

20. Inde, m'bale ndikondwera nawe mwa Ambuye: utsitsimutse mtima wanga mwa Kristu.
21. Pokhulupirirakumverakwakondikulembera iwe, podziwa kuti udzachitanso koposa chimene ndinena.

Pano pali nkhani yochititsa chidwi. Taonani Paulo akunena nkhani yakuti wokhulupirira ayenera kuchita zinthu zomwe ndi zosangalatsa ena.Kunena kuti m'busa achite zinthu zosangalatsa nkhosa zake, komanso nkhosazozisangalatsem'busayo.Kutanthauza kuti pamene wokhulupirira apeza mabvuto m'dziko, ayenera kukapezachitonthozo, mpumulo ndi chisangalalo ku mpingo. Komanso tikuona kuti chipatso cha chikhulupiriro ndi kumvera mwa anthu ndizo zimene zimasangalatsa mtumiki wa Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau a Paulo a mu verse 22-25, momwe akuyembekezakuturutsidwa m'ndende kotero kuti akufunabe mapemphero ya abale. Ndipo akumaliza kalatayi, mwakupereka moni ndi mafuno abwino.

Tere kwalerotilekeza pano. Ndipo timasanthula kalata ya Paulo kwa Filemoni momwe timakambirana za kuonetsedwa kwa chikondi cha Kristu kwa ife ndi kuonetsa momwe chikondi chapa abale chiyenera kukhalira. Tere tatsiriza kusanthula kalata imeneyi.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!